

7. Mosaonera, lembani zifukwa zisanu ndi chimodzi zakuti, kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kupemphera?

- (1) \_\_\_\_\_
- (2) \_\_\_\_\_
- (3) \_\_\_\_\_
- (4) \_\_\_\_\_
- (5) \_\_\_\_\_
- (6) \_\_\_\_\_

\*\*\*\*\*

MAYANKHO.

- 1. Anthu ena.
- 4. Kupemphera.
- 6. Ndiganiza kuti mumachita.
- 2. Iye amafuna kuti iwo apeze chipulumutso.
- 5. Mphamvu ya Mulungu siili ya ufulu kugwira ntchito.
- 3. Iye akunena za kukolola kulalikira kwa anthu ndi kuwa-bweretsa kuti atembenuke mtima.
- 7. Chifukwa Mulungu amatiuza kuti tizipemphera.  
Chifukwa Mulungu amafuna chiyanjano ndi ife.  
Chifukwa ndi mmene machimo athu amakhululukidwamo ndi mmene timagonjetsera mayesero athu.  
Chifukwa ndimo mmene timasungilamo umoyo wathu wa uzimu.  
Chifukwa ndi mmene timapezelamo zinthu zimene timazifuna  
Chifukwa pemphero limamasula mphamvu ya Mulungu kuti igwire ntchito.

SABATA LACHITATU: KODI TIYENERA KUPEMPHERA NTHAWI ITI?  
TSIKU LOYAMBA:

Sabata latha tidaphunzira zifukwa zimene ife tiyenera kupe-  
mpherera. Kodi mungathe kuzikumbukirabe? Onaninso maphu-  
nziro anu olembedwa pa Sabata la 2 Tsiku la 6. Penyani ku-  
mbali osayang'anira papepala muyese kuzinena pamtima. Were-  
nganinso pano kachiwiri. Kenaka lembani zifukwa zambiri  
monga mmene mungalembere mosayang'anira papepala.

1. Kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kupemphera?

- (1) \_\_\_\_\_
- (2) \_\_\_\_\_
- (3) \_\_\_\_\_
- (4) \_\_\_\_\_
- (5) \_\_\_\_\_
- (6) \_\_\_\_\_

=====

Mwa ichi tikuona kuti kupemphera kuli kofunika kwambiri.  
Kodi ntchito yofunika yopempherayi tiyenera kugwira liti?  
Zimenezi ndi zimene tikufuna kuti tiziphunzire sabata ino.  
Choyamba, ine ndikufuna kudziwa zimene inu mumaganiza za  
nthawi imene tingapemphere. Taganizani bwinobwino mmene  
mumakhallira pa tsiku. Taganizaninso nthawi zimene inu muma-  
pempherera.

2. Lembani nthawi zimene inu mumapemphera.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

=====

Akhristu ambiri amapemphera akangodzuka m'mawa. Iyi ndi nthawi yabwino yopemphera. Iwo amakumbukira kuti Mulungu ali nawo pamenepo. Amalankhula naye. Amamuthokoza chifukwa cha moyo ndi mphamvu. Amamupempha Iye kuti awathandize kuti akhale naye pa tsikulo.

3. Kodi muganiza kuti ndi chinthu chabwino kuti munthu alankhule ndi Mulungu kwakanthawi kochepe asanachoke m'chofunda chake?

---

=====

Nthawi ina imene Akhristu amapemphera ndiyomwe amakhala atakonzeka kuti azidya chakudya chawo. Asanayambe kudya, amamuthokoza Mulungu chifukwa chakuwapatsa chakudyachi. Ngakhale titanena mawu ambiri kapena pang'ono mpemphelori, koma liyenera kuchokeradi m'mitima mwathu.

4. Kodi kumasonyeza kuthokoza kwenikweni ngati ife tibwere-zabwereza mawu pang'ono kwa Mulungu tisanadye ndikusaganiza zimene tikunena?

---

=====

Akhristu amakondanso kumapemphera pamodzi ndi mabanja awo. M'njira imeneyi ana nawonso amaphunzira kupemphera pamene amamva makolo awo akupemphera mokwenza. Ndipo banja limakomana pamodzi pamene abweretsa zosoŵa zao kwa Mulungu.

5. Kodi ndi chifukwa chiyani pemphero la m'banja lili lofunika?

---

=====

Ndi chinthu chabwinonso kwa Mkhristu kupemphera asanapite kukagona usiku. Iye atha kuganiza zonse zimene iye wakhala akuchita pa tsikulo ndikumupempha Mulungu kuti amusonyeze zomwe zinali zabwino ndi zimene sizinali zabwino. Iye akhoza kumuthokoza Mulungu pakukhala naye ndikumupempha Mulungu kuti amusunge usiku wonse. Ngakhale pamene iye akupita ku-

kagona akhozabe mumamuthokoza Mulungu kuti iye ali naye. Mwa njira imeneyi maganizo ake omaliza amakhala pa za Mulungu, chimodzimodzinso akauka m'mawa akangotsegula maso ake maganizo ake oyamba ayenera kukhala a Mulungu.

6. Kodi mungathe kukumbukira zimene munali kuganiza usiku wathawu pamene mumapita kukagona? Nanga chinali chiyani?
- 
- =====

7. Kodi muganiza kuti mungathe kuphunzira kuganiza kapena kulankhula ndi Mulungu pamene mukupita kukagona usiku uliwonse?
- 
- =====

Kodi Buku Lopatulika limanena chiyani za nthawi yopemphera? Kodi nkwabwino kupemphera kwa nthawi yaitali? Kumbukirani.

1 Atesalonika 5:17:  
Pempherani kosalekeza.

Taonani mmene Danieli anapempherera kwa Mulungu.

Danieli 6:10:  
Ndipo podziwa Danieli kuti adatsimikiza cholembedwacho, iye analoŵa m'nyumba mwake, m'chipinda mwake, chimene mazenera ake anatseguka oloza ku Yerusalemu; ndipo anagwada maondo ake tsiku limodzi katatu, nape-  
mpherana nabvomereza pamaso pa Mulungu wake monga umo amachitira kale lonse.

8. Kodi Danieli anali kugwada ndi kupemphera kangati pa tsiku?
- 
- =====

Kuchokera m'ndime zimenezi taona kuti ndi koyenera kuti tizipemphera nthawi zambiri pa tsiku. Ngati mupemphera pamene muli kuuka, pamene muli kudya chakudya, pamene muli

kuchita mapemphero abanja lonse, ndi pamene muli kupita kugona zidzakuthandizani kuti musaiwale Mulungu.

9. Kodi muganiza kuti ndi chinthu cholimba kumapemphera nthawi zonsezi?

=====

Ayi, kupemphera nthawi zonse sichinthu chobvuta ngati mukondadi Mulungu. Kunena zoonā, tidzaona kuti pali nthawi zambiri zimene ife tiyenera kuti tizipemphera. Koma tiyeni tiyambe ndi izi. Ngati simunapempherepo nkale lomwe pa nthawi izi, mpempheni Mulungu kuti akuthandizeni kuti muzikumbukira kutero.

10. Lembani nthawi zabwino zimene Akhristu amapemphera pa tsiku lililonse.

\_\_\_\_\_

\_\_\_\_\_

=====

\*\*\*\*\*

MAYANKHO.

8. Katatu pa tsiku.
5. Limaphunzitsa ana ndikugwirizanitsa banja lonse.
3. Yankhani monga mmene mungaganizire.
9. Ngati muganiza kuti kuli kobvuta, mufunika kuti muphuzizire kwambiri za pemphero.
4. Ayi.
2. Tidzakamba za yankho lanu m'kalasi.
7. Ndiganiza mungatero.
6. Mudzayenera kuyankha nokha.
10. Pamene akuuka, asanadye chakudya, pamene akuchita mapemphero a banja lonse, pamene akupita kukagona.
1. Yang'anani pa Sabata la 3, Tsiku la 1, funso la 1, kuti mupeze mayankho ake.

SABATA LACHITATU: KODI TIYENERA KUPEMPHERA NTHAWI ITI?  
TSIKU LACHIWIWI:

Dzulo tinaphunzira kuti kuli kwabwino kwa Mkhristu kumape-  
mpha nthaŵi zina tsiku lonse la thunthu.

1. Kodi ndi nthaŵi yanji imene Mkhristu ayenera kupempha  
tsiku lililonse?

---

---

=====

Koma ngati titakumbukira kuti pemphero ndi chiyani, ndiye  
kuti tidzadziŵa kuti sichinthu chakuti chingangochitika pa  
nthaŵi zina zake zokha.

2. Kodi pemphero ndi chiyani? \_\_\_\_\_

---

=====

Pamene tikulankhula pamodzi ndi anthu, sitingolankhula nawo  
panthaŵi yosankhidwa yokha tsiku lililonse ayi. Koma tima-  
lankhula nawo nthaŵi iliyonse pamene iwo ali ndi ife. Inde,  
sitingalankhule nawo pamene ali pamalo pena.

3. Kodi mumalankhula ndi anthu katatu kapena kanayi kokha  
pa tsiku?

---

=====

Buku Lopatulika limatiuza kuti Mulungu amakhala nafe nthaŵi  
zonse. Izi ndizo zimene Yesu ananena pamene thupi lake  
lisanatengedwe kupita kumwamba. Ngakhale kuti thupi lake  
silidzaonekansa, koma Iye anati,

Mateyu 28:20:

Ndipo onani, Ine ndili pamodzi ndi inu masiku onse kufikira chimaliziro cha nthaŵi ya pansi pano.

4. Kodi Mulungu amatibwerera ndi kumatisiyanso nthaŵi zambiri tsiku lililonse?
- 
- =====

Tingathe kulankhula ndi anthu nthaŵi iliyonse pamene iwo ali ndi ife ndipo tingalankhule ndi Mulungu pamene Iye ali ndi ife.

5. Ngati Mulungu amakhala ndi ife nthaŵi zonse, nanga tingalankhule naye nthaŵi yanji?
- 
- =====

Ine ndikhulupirira kuti siganizo latsopano kwa inu. Ngati ndikadakufunsani tisanayambe phunziroli kuti, "Kodi tikhoza kulankhula ndi Mulungu nthaŵi ziti?" Mukadayankha kuti, "Tingathe kulankhula ndi Mulungu nthaŵi iliyonse." Koma chovuta chake ndi ichi ngakhale tikudziŵa zimenezi koma timaiŵala kulankhula naye. Timapemphera pa nthaŵi yake, kapena pamene tili ndi mavuto, koma timaiŵalanso kulankhula naye nthaŵi zina ngakhale kuti Iye ali ndi ife paliponse.

6. Kodi muganiza kuti mkazi wanu, kapena mwamuna wanu, kapena abwenzi anu, angamve bwanji ngati muiŵala kulankhula nawo pamene ali m'mudzi mwanu?
- 
- =====

Yesu ndiye bwenzi lathu. Iye ali ndi ife nthaŵi zonse. Iye amafuna kuti tizikumbukira kuti Iye alipo. Pamene Mulungu anapereka lonjezo kwa Abrahamu anati kwa iye, Genesis 17:1:

"Yenda iwe pamaso panga, nukhale wangwiro."

Kodi izi zikutanthauza chiyani? Njira ina yonenera mawu aŵa ndi iyi. "Khala wokumbukira nthawi zonse kuti ine ndili pompo."

7. Ngati mukukumbukira kuti Mulungu ali ndi inu nthawi zonse, kodi mukhoza kulankhula naye koposa?
- 
- =====

Ngati Mulungu ali ndi ife nthawi zonse, ndiye kuti Iye ali nafe pamene tiyenda ndiponso pamene tili kuphika. Ali nafe pamene tikulima m'munda. Ali nafe pamene tikuyendera anazathu. Ali nafe pamene tikudya, kugona pansu, kukwera njinga, kungokhala chete, kapena pamene tikulankhula ndi ana athu.

8. Kodi kungakhale kotheka kuti tizipemphera nthawi zonse-zi?
- 
- =====

Inde, tikhoza kupemphera ngakhale pamene tili kuchita chilichonse! Ndipo ndi zimene Mulungu amafuna kuti tizichita. Pamene tikuyenda tikhoza kupempherera anthu amene tili kukawaona. Pamene tili kuphika chakudya tingapempherere anthu amene akuuyembekezera kudya chakudyacho. Pamene tili kulima tingathe kuthokoza Mulungu chifukwa cha mbeu ndiponso kumpempha kuti athandize mbeuzo kuti zikule bwino.

Pamene tikukachezera anzathu, tingathe kupemphera kuti nawonso akamlandire Khristu kukhala Mpulumutsi wawo. Pamene tikhala chete tikhoza kumpempha Mulungu kuti atiphunzitse njira yeke. Pamene tilankhula ndi ana athu tikhoza kumuthokoza Mulungu chifukwa chotipatsa ife anawo ndikumpempha kuti adzionetse yekha kwa anawo.

9. Kodi tyenera kupemphera nthawi iti?
- 
- =====

\*\*\*\*\*

MAYANKHO.

7. Ndiganiza choncho.
3. Ayi. Sichoncho.
1. Pamene auka, pamene akudya chakudya, pamene achita mapemphero a banja lonse, pamene apita kukagona.
4. Ayi, ali nafe nthawi zonse.
8. Inde, ndi choncho.
5. Nthawi iliyonse.
2. Pemphero ndiko kulankhula ndi Mulungu.
6. Angakhale wodabwa ndiponso wovutika. Angaganize kuti inu mwawakwiira kapena kuti simukwakonda.
9. Nthawi iliyonse.

SABATA LACHITATU: KODI TIYENERA KUPEMPHERA NTHAWI ITI?  
TSIKU LACHITATU:

Dzulo tinaphunzira kuti sikuli kokwanira kungopemphera pa nthawi yosankhidwa yokha. Tinaphunziranso kuti Mulungu ali nafe nthawi zonse, ndipo amafuna kuti azinena nafe nthawi iliyonse.

Lero tikufuna kuphunzira pemphero labwino limene linalembe-  
dwa m'Buku Lopatulika. Tsegulani Buku lanu Lopatulika ku  
Masalmo 139. Mu mpemphero ili mudzaona m'mene Mulungu wati-  
yandikirira paliponse pamene tili. Werengani pempheroli  
pang'onopang'ono. Lankhulani naye Mulungu pamene muli kuwe-  
renga. Mukatha, lembani pamunsipa m'mene mwamvera, kapena  
mwaganizira, kapena zimene Mulungu wakuuzani pamene mumawe-  
renga.

---

---

---

---

---

---

SABATA LACHITATU: KODI TIYENERA KUPEMPHERA NTHAWI ITI?  
TSIKU LACHINAYI:

Tiyeni tiyambe lero kuganizira nthawi zimene taphunzira za mapemphero. Tinayamba kukamba za (1) nthawi zimene anthu ambiri amapemphera...monga popita kukagona, pakudya chakudya kapena pochita mapemphero a banja lonse. Ndiye tiona kuti Mulungu pokhala bwenzi lathu ndipo kuti amakhala nafe nthawi zonse, tisamangopemphera pa nthawi zokhazi komanso (2) tizipemphera nthawi iliyonse.

Koma ngakhale kuti Mulungu amafuna kuti tizilankhula naye nthawi iliyonse ngakhale pamene tikuchita chinthu china chake, komanso pali kanthu kena kamene ife tiyenera kukumbukira Timalankhula kwambiri ndi anzathu kudzanso mabanja athu pamene ife timafuna kukhala pansu pamodzi. Timafuna kutenga nthawi tikucheza kuti tipitirizebe kumvana wina ndi mnzake.

1. Kodi nthawi zina mumapempha abwenzi anu kapena banja lanu kukhala pansu ndikucheza nawo?

---

=====

Ndi chimodzimodzinso ndi Mulungu. Iye amafuna kuti tizikhala ndi nthawi ndi Iye Yekha. Sitingathe kuphunzira kumudziwa Iye bwinobwino ngati titamangonena mawu pang'ono chabe kwa Iye pamene ife tilikupanga zinthu zina. Kutu timudziwe bwino Mulungu, tiyenera kukhala ndi nthawi ina tsiku lililonse yakukhala pansu kapena kumugwadira osachita kanthu kena kalikonse koma kungolankhula naye basi.

2. Kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kukhala ndi nthawi ina tsiku lililonse ya kulekeza kuchita zinthu zina zake ndi kupemphera?

---

=====

Pamene Yesu anali kuphunzitsa ophunzira ake kupemphera Iye anati:

Mateyu 6:6:

Koma iwe popemphera, loŵa m'chipinda chako, nutseke chitseko chako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.

3. Kodi tizingopemphera pamene tikuchita zinthu zina zake tsiku la thunthu?

=====

Kupemphera pamene tikugwira ntchito ndikwabwino, koma siko-kwanira. Nthaŵi zina pa tsiku lililonse tiyenera kumapita kumalo ena opanda phokoso ndikusiya zinthu zina zonse. Pamene tikhala chonchi ndi Mulungu, tingathedi kuphunzira mukudziŵa Iye. Pa nthaŵiyi pali zinthu zambiri zoyenera kuzipempherera. Kenaka tidzakamba za zinthu zonsezi, koma pakali pano tikufuna kutsimikiza kuti tiyenera kukhala ndi nthaŵi yoleka zinthu zina ndi kumalankhula ndi Mulungu tsiku lililonse.

4. Kodi mumaganiza kuti Akhristu ambiri amachita zimenezi?

=====

Kodi muyenera kukhala ndi nthaŵi iti yokhalira panokha pamene muli ndi Mulungu? Palibe lamulo lililonse la zimenezi. Nthaŵi sikuti ili yolingana ndi munthu aliyense ayi. Mudzapeza nthaŵi imene ili yabwino kwambiri kwa inu. Kapena nthaŵi yabwino kwa inu imene mungamapemphere ndi yamadzulo pamene mwatha ntchito zanu zonse, pamene kwada usiku, ndi pamenenso ana atagona. Pamene mukhoza kutaya uko maganizo anu ena ndi kukhala pansu kapena kugwada pansu ndi kumatha nthaŵi yanu muli kulankhula ndi Mulungu kupyolera m'mape-mphero anu. Kapena nthaŵi yabwino kwambiri kwa inu ingakhale masana mutatha kudya chakudya chanu pamene musanakonzeke-re zoyambanso ntchito yanu.

5. Kodi Akhristu onse azikhala ndi nthawi imodzimidzi yopemphera?

---

=====

Koma vuto lake lopemphera madzulo ndi masana ndi lakuti timakhala otanganidwa ndi zinthu zina, kapena kuti munthu wina amabwera kudzalankhula nafe ndiye maganizo athu amaiwala zopemphera. Kotero kuti timaiwala kupemphera.

6. Kodi Mulungu ali nazo kanthu ngati ife titalephera kukhala ndi nthawi yokhala naye?

---

=====

Anthu ambiri amaona kuti nthawi yabwino kwambiri yopemphera ndi ya m'mawa pamene sanayambe ntchito iliyonse. Amauka mofulumira kusanakhale phokoso lililonse lowasokoneza iwo. Iwo amawerenga Buku Lopatulika nayamba kulankhula ndi Mulungu pa zilizonse zimene zili mumtima mwawo. Ndipo pamene iwo akupita ku ntchito amaganiza motsimikiza mtima kuti Mulungu ali nawo.

7. Kodi nthawi yabwino kwambiri kwa inu yokhala yopanda phokoso ndi iti pakati popemphera, masana, kapena madzulo, kapena m'mawa?

---

=====

Mungathe kusankha nthawi yanu. Koma mukasankha, muyenera kuisunga mosamala tsiku lililonse. Osalola zinthu zina kuti zitenge malo ake. Osaiwala. Osadzipanga kukhala otanganidwa pa nthawi imeneyi. Ngati muphonya mudzaona ngati Mulungu ali patali ndipo mudzakhala ofooka pa moyo wa Chikhristu.

8. Tsopano ndikufunsi ndipo mundiyankhe mwachilungamo. Sichidzakuthandizani kunena chinthu chonama. Ngati munena zoonazidzakuthandizani kuona m'mene moyo wanu wa Chikhristu uliri. Kodi mumakhala ndi nthawi yapadera yokhala

pansi, kapena kugwada ndi kumapemphera?

---

=====

Pano ndiye poyambira. Dzipanikizeni nokha. Sankhani nthawi ndipo muyenera kuisunga tsiku lililonse. Ngati nthawi zina mulephera, mpempheni Mulungu kuti akukhululukireni, ndipo muyesenso maŵa. Mulungu adzakuthandizani pa ichi ngati mutafunitsitsadi kutero.

9. Kodi tiyenera kukumana naye Mulungu m'njira yotani tsiku lililonse?

---

=====

\*\*\*\*\*

MAYANKHO.

7. Mudzadziyankhira nokha zimenezi.
3. Ayi, sikuli kokwanira.
5. Ayi, nthawi zawo zidzakhala zosiyana.
9. Tiyenera kupeza malo opanda phokoso kukhala nthawi tili ndi Mulungu.
  1. Ndiganiza mumatero.
  8. Apanso muyenera kuti mudziyankhire nokha.
  2. Chifukwa ndi njira yokhayo imene tingathe kudziwira Mulungu bwino.
  6. Inde zimadandaulitsa iye koposa m'mene zimakhalira kwa anzathu ngati sitikhala pansi ndikulankhula nawo.
  4. Ndinafunsa zomwe mumaganiza choncho yankho lanu lili lokhoza, koma kwa ine, ndili ndi mantha Akhristu ambiri sakhala ndi nthawi imeneyi yopemphera.

SABATA LACHITATU: KODI TIYENERA KUPEMPHERA NTHAWI ITI?  
TSIKU LACHISANU:

Sabata ino taona kuti sikuli kokwanira kungopemphera pang'ono m'mawa ndi madzulo, kaya pamene tili kudya, kapena pamene tili kuchita mapemphero a banja lathu lonse. Taonanso kuti ngakhale kuti zili bwino kumalankhula ndi Mulungu nthawi iliyonse pamene tili kugwira ntchito, kapena paulendo, ukunso sikuli kokwanira ayi. Sitingaphunziredi kumudziwa Mulungu mwa njira imeneyi.

1. Kodi tizipemphera bwanji kuti tiphunzire kumudziwa bwino Mulungu?
- 
- =====

Tsopano tiyeni tipeze nthawi ina yakuti tizipemphera. Tawerengani ndime izi kenaka pamene tikukamba za ndimezi mungaŵerengenso.

Numeri 16:22:

Ndipo anagwa nkhope zawo pansi, nati, "Mulungu, ndinu Mulungu wa mizimu ya anthu onse, walakwa munthu m'modzi, ndipo kodi mukwiya nalo khamu lonse?"

1 Samuel 1:10:

Ndipo mkaziyo (Hana) anali ndi mtima woŵawa nape-  
mphera kwa Yehova, naliratu misonzi.

Ezara 9:5:

Ndi pa nsembe yamadzulo ndinanyamuka m'kuzunzika kwanga, chovala changa ndi malaya anga zong'ambika; ndipo ndinagwada ndi maondo anga, ndikutambasula manja anga kwa Yehova Mulungu wanga.

Luka 6:12-13:

Ndipo kunali masiku aŵa, Iye anatuluka nanka kuphiri kukapemphera; nachezera usiku wonse m'kupemphera kwa Mulungu. Ndipo kutacha, anaitana ophunzira ake; nasankha mwa iwo khumi ndi aŵiri, amene anaŵachanso

dzina lawo lakuti atumwi.

Mateyu 26:39:

Ndipo anamuka patsogolo pang'ono, nagwa nkhope yake pansu, napemphera, nati, "Atate, ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire ine, koma simonga ndifuna ine, koma inu."

Machitidwe 12:5:

Pamenepo ndipo Petro anasungika m'ndende, koma Eklesia anampempherera iye kwa Mulungu kosalekeza.

Machitidwe 13:3:

Pamenepo, mmene adasala chakudya ndikupemphera ndi kuika manja pa iwo, anaŵatumiza amuke.

2. Kodi anthu ameneŵa amatani m'ndime zonsezi?

---

3. Nanga ndi chifukwa chiyani iwo amachita zimenezi?

---

=====

Inde, pa nthawi imene pamaoneka bvuto, anthu a Mulungu amaganizira zopemphera. Umo ndimo mmene ziyenera kukhalira. Mulungu amasamala miyoyo yathu ndipo nthawi zonse ngati pali chofunika chachikulu Iye amafuna kutithandiza. Koma kumbukirani kuti Iye amafuna tizipempha chithandizo.

4. Monga mmene tikuoneramu ndime izi, kodi nthawi ina imene tiyenera kupemphera ndi iti?

---

=====

Choncho kupatulako nthawi zimene timapemphera tsiku lililonse, pali nthawi zinanso zazikulu zimene tiyenera kumapemphera. Izi sizingotanthauza nthawi iliyonse pamene pali bvuto, kapena chinthu china choipa chikationekeranso ife ayi

Onani pa Machitidwe 13:3. Timawerenga kuti anthu anasala chakudya nayamba kupemphera pamene anali kutumiza Paulo ndi Barnaba monga a mishoni. Onaninso pa Luka 6:12-13. Yesu anapemphera usiku wonse pamene anali pafupi kusankha atumwi ake khumi ndi awiri. Chimodzimodzi ifenso tiyenera kukhala nthawi yapadera yopempherera zinthu zazikuluzikulu za m'mi-yoyu mwathu.

5. Talembani chinthu chachikulu m'moyo mwanu chimene muganiza kuti mungachitayire nthawi yapadera pa mapemphero anu.

---

Nthawi zina tiyenera kukhala ndi nthawi yopempherera zosowa zathu zazikuluzikulu zimene tili nazo. Mnyamata sangathe kusankha mkazi wakuti amukwatire pokhapokha choyamba atakhala panso ndi kupemphera nthawi yaitali. Mlalikinso sayenera kupita kukalalikira pokhapokha atayamba wapeza nthawi yopemphera yekha. Izi zingakhale zopyolera mphindi zochepa m'mawa kapena madzulo. Chingakhale chopambana kwambiri kulankhula ndi Mulungu pamene tikugwira ntchito zathu. Chingakhalenso chopambana kwambiri kugwada panso kwa inu nokha kwa kanthawi.

6. Pa Luka 6:12-13, kodi Yesu adapemphera kwa nthawi yaitali bwanji asanasankhe ophunzira ake aja okwanira khumi ndi awiriwa?

---

Anthu ena amene ali mu ndimezi anali kupeza mavvuto oopsya. Pa 1 Samueli 1:10, Hana anali osabala. Pa Ezara 9:9, Ezara anasenzetsedwa chikatundu cholemera kwambiri chifukwa chachimo a anthu. Pa Numeri 16:22, ana a Israyeli anali kupemphera chifukwa chakuti Kora anamuukira Mulungu ndipo anthu onse akanalangiwa.

7. Imodzi mwa ndime zimene tawerengazi inali Mateyu 26:39. Tatsegula Buku Lopatulika pa mutu umenewu. Werengani kuchokera ndime 36 mpaka 39 ndipo munene chifukwa chake

chimene Yesu anabvutikira pa nthaŵi imeneyi.

---

=====

Pali zinthu zina zake zimene ife sitingangozipempherera pa nthaŵi yochepa yokha. Tiyenera kukhala ndi nthaŵi yapadera yozipempherera zinthu zimenezi. Ndipo tiyenera kupitirizabe kupemphera.

8. Taonani pa Machitidwe 12:5, zimene tawerenga. Kodi mpingo unampempherera bwanji Petro pamene anali m'nde-nde?
- 
- =====

Kodi tiyenera kupemphera nthaŵi iti? Tiyenera kupemphera pamene tikuuka ndi pamene tikugona, m'mapemphero a banja lonse ndi pakudya chakudya. Tiyenera kupemphera pamene tikugwira ntchito. Tiyenera kupeza nthaŵi yapadera tsiku lililonse yokhala panso kapena kugwada ndi kumalankhula ndi Mulungu kupyolera m'mapemphero athu.

9. Monga mmene taphunzirira m'phunziro lathu la lero, kodi nthaŵi ina imene tiyenera kumapemphera ndi iti?
- 
- =====

Ife tsopano tanenapo za nthaŵi zinayi zosiyana popemphera. Muwerengenso nthaŵizi ndipo muyesetse kukumbukira pamtima.

- (1) Podzuka, pogona, pakudya chakudya kapena kukhala ndi mapemphero apabanja.
- (2) Nthaŵi iliyonse masana pamene mukugwira ntchito.
- (3) Pa nthaŵi yosankhidwa tsiku lililonse pamene mwasiya ntchito zonse ndi pamene kuli zii kopanda phokoso muli nokha pamaso pa Mulungu.
- (4) Pamene muli ndi chofunika chachikulu m'moyo mwanu.

\*\*\*\*\*

### MAYANKHO.

3. Mukhoza kupereka mayankho ambiri pano.  
Anthu aŵa anapemphera pa zifukwa zosiyanasiyana, koma ambiri aiwo anali kupemphera chifukwa chakuti anali ndi zosoŵa zazikulu, kapena mabvuto a m'miyoyo mwawo.
1. Pakupeza nthawi tsiku lililonse yosiya zina zonse ndi kukhala pa nokha muli kupemphera.
8. Iwo anakhala akumpempherera kolimbika.
6. Usiku wonse.
4. Pamene tili ndi zosoŵa, kapena ngati china chake chachikulu chikuchitika m'miyoyo mwathu.
2. Anali kupemphera.
9. Pamene tili ndi mavuto kapena chosoŵa chachikulu kapena china chake chachikulu m'miyoyo mwathu.
2. Anali kupemphera.
9. Pamene tili ndi mabvuto kapena chosoŵa chachikulu kapena china chake chachikulu m'miyoyo mwathu.
7. Inali pafupifupi nthawi yake yakufa.
5. Ichi chingakhale chinthu chilichonse chimene munga-chiganizire...monga pamene anthu akukuzondani, kapena ngati paoneka maliro m'banja, kapena pamene muli tchimo mumpingo, kapena pamene muli kudwala, kapena zinthu zina zake.